



didacoeilho.com

# KODI FOTELEZA WA CHILENGEDWE NDI CHANI?

**F**oteleza wa chilengedwe amapangidwa kuchokela ku zipangizo zimene zimapangidwa mwaizo zokha mu chilengedwe, kuphatikizapo **bio-fertilizer, kompositi**, komanso **manyowa wochokela ku zinthu za ziwisi ndi aziweto**. Zimathandizila kukula kwa mbeu komanso kukonza nthaka mkupita kwa nthawi mwa **pang'onopang'ono** kumapeleka Michere yofunikila mu nthaka.

- **Bio-fertilizer** amapangidwa kuchokela ku zinthu zimene ndi (zochokela ku) zamoyo m'mene muli tizilombo ting'onoting'ono tofunikila pa makulidwe a zomela.
- **Kompositi** ndi zinyatsi zowolelana – zamasamba kapena manyowa.
- **Manyowa wochokela ku zinthu za ziwisi** ndi mbeu yodzididwa kenako kudulidwa ndi kuphatikizidwa mu nthaka, zimene zimawonjezela zinyatsi komanso kupeleka michere yofunikila ku mbeu. Zimathandizanso kusunga chinyontho mu nthaka.
- **Manyowa a organic** amapangidwa kuchokela ku zinthu zochokela ku nyama zimene zikuwolelana monga zidutsa za mafupa, ndowe, ntope (chiphatikizo cha manyowa ndi madzi), komanso manyowa wochokela ku mbalame za kunyanja ndi mileme.

Mitundu yambiri ya foteleza wa chilengedwe ndi yopezekelatu, ya ulele, yopezeke pa munda wanu komanso ku nyumba kwanu ndinso ku ziweto zanu.

